


abvomereza kutengapo chipulumutso. Pakuti, amene aliyense adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka." Kodi mukhulupirira mu mtima mwanu kuti Mulungu anatuma Yesu kudzafera pa mtanda chifukwa cha machimo anu, anayikidwa m'manda, nawukitsidwa kwa akufa kuti inu mulungamitsidwe. Kodi ndi pakamwa panu mungachilengeze ichi? Ngati mungathe, tsopano Mulungu adzakutchani wopulumutsidwa.

Pali miyoyo yambiri ya mtengo wapatali yomwe imaganiza kuti ndiyopanda phindu, Koma izi sizoona ai. Pa zolengedwa zonse, inu ndinu wofunika kwambiri kwa Mulungu, ndipo anatsimikizira izi potumiza mwana wache kudzafa m'malo mwanu. Ngati muli ofuna kukhulupirira Yesu Khristu ngati mpulumutsi wanu, bwanji wosapezerapo mwai pa nthawi yomwe yino kumuyamika pokusamalirani ndi kumfunsa kuti alowe mu m'tima mwanu. Lolani pemphero lanu lichokere mu mtima woona ndi wosweka.



P.O. BOX 1115 • YORK, SC 29745 • 803-684-1535
WWW.HOPETRACTS.ORG
What Is The Most Important Thing? (Chichewa) Tract 531



**KODI CHOFUNIKA
KWAMBIRI NCHIYANI
PA DZIKO LAPANSI?**

Kodi munayamba mwaganizira za chinthu chomwe Mulungu amachiona kuti ndi chofunikira kwambiri pa dziko lapansi? Kodi ndi golidi ndi siliva, chuma chomwe munthu ali nacho, kukongola kwa malo wochititsa chidwi, anthu otchuka kwambiri kapena kudziwika, komanso machitidwe a munthu wandale? Kodi chingakhale nzeru za wa sayansi, malankhulidwe a munthu wodziwa kulankhula, kapena malo otchuka a maphunziro? Ntheradi, sizinthu izi ai!

Ndi zonna kuti "Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi koteri, kuti anapatsa Mwana wache wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira lye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha." (Yohane 3:16) Ndi zoonanso kuti "Pakuti Mwana wa munthu anadza kufunafuna ndi kupulumutsa chotayikacho." (Luka 19:10) chimodzimodzinso "Pakuti onse anachimwa, naperevera pa ulemerero wa Mulungu;" (Aroma 3:23)

Mulungu akunenanso kuti "Ameneyo sanadziwa uchimo anamyesera uchimo m'malo mwathu; kuti ife tikhale chilungamo cha Mulungu mwa lye." (2 Akorinto 5:21) chifukwa cha ichi, kunena moona mtima, munthu ndiye chinthu chofunika kwambiri kwa Mulungu. Choncho, Mulungu akufuna uthenga wabwino wa Ambuye Yesu upatsidwe m'dzanja la wina aliyense, bambo, mai, m'nyamata, mtsikana padziko lonse lapansi. Ambuye akupatsani gawo ili la mau m'dzanja lanu kuti muwerenge ndi kukhazikika m'moyo wanu.

Okondedwa, "Ambuye sazengereza nalo lonjezano, monga ena achiyesa chizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa." (2 Petro 3:9) Ndinu wofunikira kwambiri. Ndi Mulungu yekha amene akudziwa ubwino wa kumwamba komanso kuipa kwa ku Gahena. Ndi Mulungu yekha amene angakupulumutseni ku Gahena ndikupita nanu kumwamba. Wina asakutengeni ngati ndinu 'opanda ntchito' pa moyo wanu, chifukwa Mulungu ali nanu ntchito yayikulu. "Pakuti munthu apindulanji akadzilemezera dziko lonse, natayapo moyo wache? Pakuti munthu akapereka chiani chosintha nacho moyo wache?" (Marko 8:36,37)

Ndinu ofunika kwambiri kwa Mulungu ndipo anapereka zonse anali nazo kuti inu mukhale ndi mwai wokhala ndi moyo wosatha kumwamba. Yesu anati ku Yohane 1:12 "Koma onse amene anamlandira lye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lache;" Kodi mumlandira lye?

Ku Mateyu 11:28 akunenanso kuti, "Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupulumutsani inu." Kodi mubwera kwa lye? Kwa Aroma 10:9,10,13 tikuwuzidwa "kuti ngati udzabvomereza m'kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mu mtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka: pakuti ndi mtima munthu akhulupirira kutengapo chilungamo; ndi m'kamwa